



M'busa Tony Alamo

IDZANI KWA KHRISTU

Yolembedwa ndi Tony Alamo

Mu Luka 21:36, Yesu akuchenjeza dziko lonse kukhala tcheru ndi “kupemphera nthawi zonse, kuti mukhale olimbika ndi kupulumuka muzonsezi zimene zidzachitika, ndi kuimilira pamaso pa MWANA WA MUNTHU.” Kodi muli angwiwo kupulumuka zimene Yesu akunena kuti zidzabwera pa dziko lapansi? Werengani chaputara 21 cha Luka ndipo muona kuti Yerusalemu anaonongedwa ndi Mfumu Taitasi, ndipo tsopano pa mapeto a nthawi, Satana, mdierekezi, ali ndi mkwiyo waukulu podziwa kuti wangotsala ndi kanthawi kochepa (Chivumbulutso 12:12)!

Yesu ati, “Inde kotero inunso, pakuna zinthu izi zili kuchitika, zindikirani kuti ufumu wa Mulungu uli pafupi. Indetu ndinena ndi inu, M'badwo uno sudzatha, kufikira zonse zitachitika. Kumwamba ndi dziko lapansi zidzatha: koma MAU ANGA sadzatha. Koma mudziyang'anire nokha, kuti kapena mitima yanu ingalemetsedwe ndi [kuchulukuka, kwa zakudya, mankhwala ozunguza bongo, mowa, chiwerewere, kapena chili chonse] chonyanya, ndi kuledzera, ndi zosamalira za moyo uno [monga kusapemphera nthawi zonse, kapena kusatetezana, kusachitira umboni], ndi kuti tsiku ilo lingafikire inu modzidzimutsa. Ngati

msampha lidzatero ndi kufikira anthu onse akukhala pankhope pa dziko lonse lapansi. [Tsopano Yesu akunena chifukwa chimene aliyense akuyenera, mosalephera, kupemphera nthawi zonse. Kenanso] Koma inu dikirani, ndi KUPEMPHERA NYENGO ZONSE [chifukwa chiyani?], kuti mukhale olimbika ndi kupulumuka muzonsezi zimene zidzachitika, ndi kuimilira pamaso pa Mwana wa munthu” (Luka 21:31-36).

“Ndipo pamene panali madzulo, ophunzira Ake anafika kwa Iye [Yesu], nanena, Malo ano nga chipululu [ngati kuti Iye samadziwa], ndipo nthawi yapita tsopano; kauzeni makamuwo amuke, apite ku midzi, kukadzigulira okha kamba [chakudya]. Koma Yesu anati kwa iwo, Iwo alibe chifukwa cha kumukira; apatseni ndinu adye. Koma iwo anati kwa Iye, Ife tili ndi mikate isanu, ndi nsomba ziwiri basi. Ndipo Iye anati, Mudze nazo kuno kwa Ine. Ndipo Iye analamulira makamu a anthu akhale pansu pa maudzu, ndipo Iye anatenga mikate isanuyo, ndi nsomba ziwirizo, ndipo m'mene anayang'ana Kumwamba, Iye anadalitsa, nanyema, napatsa mikateyo kwa ophunzira Ake, ndipo ophunzira anapatsa kwa makamuwo. Ndipo anadya onse, nakhuta: ndipo anatola makombo otsala mitanga khumi ndi iwiri yodzala. Ndipo anadyawo anali amuna monga zikwi zisanu, osawerengera akazi ndi ana. Ndipo pomwepo Yesu anaka-

kamiza [kukakamiza, kuimiliza, kapena kupangitsa] ophunzira Ake kulowa m'ngalawa, ndi kutsogola Iye asananyamuke kupita ku tsidya lina, kufikira Iye atauza makamuwo amuke. Ndipo pamene Iye anawauza makamuwo kumuka, Iye anakwera m'phiri pa yekha kukapemphera [YESU, amene ali Mzimu wa Mulungu wathupi, ANAPITA KUKAPEMPHERA]: ndipo pamene panali madzulo, Iye anakhala kumeneko yekha” (Mateyu 14:15-23).

“Chifukwa chake ngati munaukitsidwa pamodzi ndi Khristu, [pamene mukupemphera] funani zakumwamba, [kuchokera] kumene Khristu wakhala ku dzanja lamanja la Mulungu,” monga kugonjetsa Satana, kuti adani athu—amene amadana nafe—akapulumuke (Akolose 3:1).

Pamene mukupemphera za kugonjetsa mdierekezi, mdierekezi amayesetsa kuchita chili chonse mu mphamvu zake kukusokonezani maganizo anu kapena kukukumbutsani zachabe zimene munachita m'mbuyo.¹ Mdierekezi amagwirira ntchito pa maganizo anu akale, amene, ngati mwapitako, amafoola kuthekera kwanu, kapenanso kukupangitsani kulopheleratu kuti mupambane zimene mukupemphelera kuti mulandire. Ichi ndi chifukwa chake Akolose 3:2-3 imatiuza ku,

(Yapitirira patsamba 2)

¹ Marko 4:15, Aef. 4:21-24, 27

IDZANI KWA KHRISTU

(Yachokera patsamba 1)

“Lingalira za zakumwamba, [pa Ambuye othekera kukupatsani chigonjetso chimene mukufuna], osati pa zinthu za padziko ayi [kapena maganizo akale, kapena zinthu zapadziko zatsopano zimene zili pa dziko lapansi! Chifukwa tikuyenera ‘kufa’ ku zinthu za kale lathu loipa ndi panopa²]. Pakuti munafa [ndi Khristu ku thupi, kwa Satana, kuti Satana asapitilize kukugwiritsani ntchito ngati] moyo wanu wabisika ndi Khristu mwa Mulungu.”

Kenako, “Pamene Khristu, amene [tso-pano] ndiye moyo wathu, adzaoneka, pamene inunso mudzaonekera pamodzi ndi Iye m’ulemelo. Nyazitsani [kutanthauza kuti, iphani mwa Uzimu] ziwalo zanu za padziko; dama, chidetso, chifunitso cha manyazi, chilakolako choipa, ndi chisiro, chimene chili kupembedza mafano [chifukwa maganizo anu ali pa tchimo mmalo mwa Mulungu, kumene kuli kupembedza mafano]: Chifukwa cha izi zomwe ukudza mkwiyo wa Mulungu pa ana a kusamvera” (Akolose 3:4-6). Pamene mukupemphera kapena ulingalira za kumwamba, mdier-ekezi adzakuyesani ndi tchimo.³

Aroma 13:1 akunena kuti, “Anthu onse amvere maulamuliro a akulu [Ambuye amene ali Mawu a Mulungu, ndi atumiki a Mulungu—amene aphunzitsa ndi kulalikira mawu a Mulungu—ndi atsogoleri amene Mulungu anawadzodza ubusa]. Pakuti palibe ulamuliro wina koma wocho-kerwa kwa Mulungu: ndipo iwo amene alipo [mu uzimu] aikidwa ndi Mulungu.”

Boma la usatana, lopanda umulungu limalola zipembedzo zabodza kuti zizichemeredwa ndi kulalikidwa m’masukulu a boma, koma silimalora Yesu, Mawu a Mulungu, kutchulidwa.⁴ Ma Baibulo onse atsopano alibe umulungu, ma Baibulo a boma ausatana, amene amakuuzani za mphamvu zilipo ndi boma lopanda umulungu.⁵ Amati palibe amene ali wabwino nthawi zonse, kuti ngakhale utapulumsidwa ndi mwana wa Mulungu, mudakalibe wochimwa, mmalo mwa cholengedwa cha tso-pano mwa Khristu Yesu ndiponso, mwana wa Mulungu.⁶ Inde, tisanapulumsidwe, tonse tinachimwa ndi kutalikirwa ulemelo wa Mulungu, koma titasinthika, siifenso ochimwa, ngati timvera Mawu a Mulun-

gu; tonse ndife zolengedwa zatsopano, ana amuna ndi akazi a Mulungu.⁷

Ma Baibulo atsopano ali ndi chikhulupiliro chonama mwa iwo chokwanira kuononga moyo wanu.⁸ Amanena mochenjera kuti Yesu amachiritsa, amaukitsa anthu akufa; amawal-amula anthu kupemphera ndi kufuna Ambuye, koma amati, MUDAKALI OCHIMWA, ndipo kuti SIMUNGAKHALE ABWINO KWAMBIRI MONGA MULUNGU AL-AMULIRA kuti mukuyenera kukhala abwino kwambiri (Genesis 17:1, Detronomy 18:13, Mateyu 5:48),⁹ ndipo kuti boma la dziko lonse la Satana ndi mphamvu ya Mulungu, pomwe Baibulo likutiiza momveka bwino kuti ndi boma la mdier-ekezi, ndi kuti limatsogole-redwa ndi mdier-ekezi (Chivumbulutso 12:9, 13:2, 4).¹⁰ pali mphamvu ziwiri—zabwino ndi zoipa. Boma, dongosolo la sukulu, kufalitsa nkhani, ndi zipembedzo za lero ndi zausatana!

Chivumbulutso 13:2 ndi 4 akuti chinjoka chimene chili mdier-ekezi ndi Satana ndi amene akupereka mphamvu zake zofooka ndi zopemphetsa ku dziko la boma limodzi la lero la Roma Katolika Vatican, loipa, landale, losatsata Yesu, losatsata Baibulo la KJV. Ndi chifukwa chiyani mukuganiza kuti Baibulo la chilungamo silitetezedwa ndi malamulo? Bwanji mumaganiza kuti a Khristu aku Waco, Texas, anaphedwa ndi awa otchedwa boma la U.S.? Ndipo bwanji mukuganiza kuti ndili mu ndende? Ndipo bwanji akunena kuti ndine owopsa—owopsa kwambiri mpaka kuti boma likuletsa anthu kubwera ku tchalitchi changa? Bwanji atenga ana athu, kuwaika mmalo osamalira ana, kuwakakamiza kupita ku masukulu achabechabe a boma, ndi kuwapangitsa adopti ndi cholinga choti azikagwiritsidwa ntchito za chiwerewere chopanga amuna kapena akazi okhaokha? Chifukwa chake n’chakuti ine ndi tchalitchi changa takhala tikulalikira za Baibulo loona, osati ma Baibulo a boma la Vatican la Roma Katolika. Alibe nazo ntchito kuti ma Baibulo atsopano ali m’masukulu, chifukwa iwo ndi amodzi mwa zifukwa zikuluzikulu zimene dziko lonse lapusitsidwa (Chivumbulutso 12:9).

Werengani Baibulo la King James Version lokha, osati King James Version watsopano. Dziwani kuti ndinu obadwanso mwatsopano, mfumu, mwana wa mwamuna kapena wamkazi wa Mulungu, wansembe, ndi wopanda tchimo.¹¹ Ngati munachimwapo m’mbuyomu mosazindikira, ndiye kuti Mulungu akukhululuki-

rani, ngati mukhulupilira Mulungu mmalo mwa mwano, usatana, boma lopanda umulungu limene linapatsidwa mphamvu zake (mphamvu za kunama, kuba, kupha, kuzunza) kuchokera kwa mdier-ekezi.¹² Osalingalira pa zinthu za pansu, koma lingalirani pa zinthu za kumwamba, osati pa zinthu za padziko (Akolose 3:2).

Mdier-ekezi amadziwa monganso adziwira Mulungu kuti dziko limakonda mdima kuposa kuwala, kuwala kwa Mulungu, amene ali Mawu a Mulungu, amene ali Yesu. Yohane 3:19 akutiiza ife chifukwa chimene dziko limadana ndi chi Khristu choona ndi Baibulo loona la KJV lakale. “Ndipo chiweruzo ndi ichi [cha dziko], kuwala [Mawu a Mulungu mwa thupi la munthu—Yesu] kwafika m’dziko, ndipo anthu [a m’dziko] akonda mdima m’malu mwa kuwala [chifukwa chiyani?], pakuti ntchito zawo n’zoipa [mpakana pano]. Amene amachita zinthu zoipa [monga boma lotsutsana ndi Khristu la lero] amadana ndi kuwala [Mawu a Mulungu a choonadi], ndipo safika pamene pali kuwala, kuti ntchito zake zisadzuzulidwe. Koma amene amachita chimene chili chabwino amabwera pamene pali kuwala [Mawu a Mulungu a choonadi], kuti ntchito zake zionekere, kuti anazichita mogwirizana [kubweretsedwa] ndi chifuniro cha Mulungu” (Yohane 3:19-21).

Choncho zochita za anthu a uMulungu ndi kuwerenga Mawu a Mulungu ndi kupemphera masana ndi usiku, kosalekeza.¹³ “Kupemphera nthawi zonse pa chochitika chilichonse mu Mzimu, ndipo khalani maso mosalekeza ndi kupemphera mopembedzera m’malu mwa oyera onse; Kuphatikizapo ineyo, ndipo chitani zimenezi kuti ndikatsegula pakamwa panga kuti ndilankhule, ndizitha kulankhula mwaufulu, kuti ndidziwitse ena chinsinsi chopatulika cha uthenga wabwino” (Aefeso 6:18-19).

“Koma mapeto a zinthu zonse ayandikira: choncho khalani oganiza bwino, ndipo khalani maso kuti musanyalanyaze kupemphera. Koposa zonse [kuposa chili chonse] khalani okondana kwambiri [chikondi, kutanthauza kusunga malamulo onse pa wina ndi mzake, aliyense¹⁴] pakati panu: pakuti chithandizo [chikondi cha uMulungu] chidzakwilira machimo ochuluka” (1 Petro 4:7-8).

“Pemphero lachikhulupiriro lidzachiritsa wodwalayo, ndipo Ambuye adzamudzutsa; ndipo ngati anachita machimo [mosazindikira, ndiye kuti Mulungu akukhululuki-

(Yapitirira patsamba 4)

2 Aro. 6:1-13, Agal. 2:20, 5:17-21, Afil. 3:7-14, Akol. 2:10-15, 2 Tim. 2:11-12 3 Yakobo 1:13-15 4 2 Tim. 4:3-4 5 Aro. 13:1-6 6 Yoh. 1:12, Aro. 6:1-7, 7:5-6, 8:14, 2 Akol. 5:17, 1 Yoh. 3:7-9 7 Yoh. 1:12, Aro. 3:23, 8:13-17, Agal. 4:4-7, Aef. 4:22-24, 1 Yoh. 3:1-2 8 Agal. 5:9 9 1 Maf. 8:61, 1 Mbi. 28:9, Yobu 1:8, Mas. 101:6, Yoh. 17:23, 2 Akol. 13:11, Akol. 1:28, 2 Tim. 3:13-17, Yakobo 1:4, 1 Pet. 5:10 10 Yes. 14:9-17 11 2 Akor. 5:16-21, 6:16-18, Chiv. 1:5-6 12 Yoh. 10:10, Chiv. 13:4 13 Yos. 1:8, Masa. 1:1-3, Luka 18:1, 21:36, 1 Ates. 5:17, 2 Tim. 2:15, 3:15-17 14 Yoh. 15:10, 1 Yoh. 2:4, 5:2-3, 2 Yoh. 6

Makalata opita kwa M'busa Alamo

India

Okonedwa M'bale Tony Alamo,

Chisomo ndi mtendere zikhale kwa inu m'dzina lolemekezeka ndi la chifundo la Ambuye ndi Mpulumutsi wathu, Yesu Khristu.

Posachedwapa tinalandira bokosi la zolemba zanu zotchedwa, "Mafupa Owuma" ndi "Chivomerezi." Tinasangalala nazo kwambiri. Tikuthokoza kwambiri chifukwa cha thandizo lanu lalikulu pothandiza kuti miyoyo yambiri yotaika ipulumutsidwe ku India.

Monga gulu la abusa 15, tinagawa kale zolemba zanu za mphamvu kwa anthu a m'madera mwathu m'misika. Tinapulumutsa miyoyo yokwana 50 chifukwa chogawa zolemba zanu. Alemekezeke Ambuye! Hallelujah!

Tikukupemphani chonde muzititumizira zolemba zanu mosalekeza.

Mulungu akudalitseni ndi kukusungani mu chasamaliro Chake, pokugwiritsani ntchito ngati chida cha mphamvu ku ulemelero wa Wamphamvu Zonse. Chonde tithandizeni m'mapemphero pa ntchito za Ambuye zomwe tikuchita ku India.

Wantchito wa Mulungu,
Reverend S.V. Rao

Ainapuram, India



M'busa Dana Kumar ndi timu ya zogawa, Tanuku, Andhra Pradesh, India

Mexico

(Zotanthauzidwa kuchoka ku Spanish)

M'busa Tony,

Moni kwa inu ndi banja lanu.

Ndafuna kukuthokozani kwambiri chifukwa cha umboni wanu komanso chifukwa cha chifundo chanu pa anthu. Ndinu m'busa owonadi chifukwa ndinu osankhidwa ndi Mulungu. Tili ndi chikhulupiliro ndikutha kuona kuti mumalalikira Mawu a Mulungu 100% ndi moonadi mmene aliri. Ndinu mtumiki wa Mulungu wa Mphamvu Zonse.

Ndife okondwa kwambiri chifukwa kudzera mwa inu tapulumutsidwa. Tikuthokoza inu ndi Ambuye. Ambuye azikutetezana tsiku lili lonse.

Mwamsangala,

Mario Garcia

Chiapas, Mexico

P.S. Mkazi wanga Isabelo nayenso akukupatsani moni.

Thailand

Mneneri wa Mulungu,

Kukuuzani zoonza, kudzodza kwa zipangizo za uzimuzi ndi kwakukulu ndi kodabwitsa kwambiri, kwabweretsa mphepo ya kusintha m'miyoyo yathu. Tikuyamba kuona ntchito zabwino za manja a Mulungu pakati pathu, kuyambira tsiku lomwe tinalandira chakudya cha uzimuchi kuchokera kwa inu. Ngakhalenso m'bale mmodzi mwa a Khristu yemwe mlandu wake umadikilira ku kotho atapempha chigamulo chachiwiri anamasulidwa, matamando apite kwa Mulungu!

Chonde, mwa ulemu ndi kulemekeza, ndikulemba kuti ndipemphe zolemba zina, ngati ndikotheka. Mulungu akupatseni mphamvu kuti muvomereze pempho langa.

Ambuye wanga, Mulungu wathu akupatsani kuthekera konse kuti mupitirize ntchito yodabwitsa pano pa dziko. Ndidzakuuzani za mlandu wanga mu kalata yanga yotsatira. Ndikukufunirani inu, banja lanu, ndi mamembala onse a Tony Alamo Christians Ministries chisangalalo, umoyo wabwino, ndi kuthekera. Madalitso ambiri a Mulungu akhale nanu, okonedwa wanga M'busa Tony Alamo, ndi mautumiki anu. Ndikuyembekezera kumva kuchochera kwa inu.

Mwana wanu mwa Khristu,
Judge Williams
Bangkok, Thailand

New Hampshire

Moni M'busa Alamo!

Ndikukulemberaninso chifukwa ndikufuna inu mudziwe za mmene inu mwakhalira mdalitso ku moyo wanga. Ndimakondwera ndikamamva za uthenga wanu pa walesi. Inu (Mulungu kudzera mwa inu) mumadyetsa moyo wanga!!

Ndinakumvani mukutchula za Vatican. Ndithu M'busa, mukunena zoonadi za Rome, Vatican ndi gulu la Chiyanjano cha Yesu (Jesuits). Ndine okondwa chifukwa sindine wa chipembedzo cha upandu!! Ndipitiriza kukupemphererani pamodzi ndi utumiki wanu. Mulungu akudalitseni kopambana!

Chikondi mwa Khristu,
Kellie Cota

Londonderry, NH



MAUTUMIKI A ALAMO PA INTANET

www.alamoministries.com

IDZANI KWA KHRISTU

(Yachokera patsamba 2)

dikira], adzakhululukidwa. Choncho muulirane machimo anu poyera, ndi kupemphererana, kuti muchiritsidwe. Pemphero la mphamvu la munthu wolungama limagwira ntchito mwamphamvu kwambiri. Eliya anali munthu monga ife tomwe, komabe anapemphera kuti mvula isagwe: ndipo mvula sinagwe kumeneko kwa zaka zitatu ndi miyezi 6. Anapempheranso, ndipo mvula inagwa kuchokera kumwamba, ndipo nthaka inatulutsa zipatso zake. Abale anga, ngati wina mwa inu wasocheretsedwa pa choonadi [mwa kusazindikira], wina n'kumubweza; Mudziwitseni, kuti amene wabweza wochimwa panjira yake yoipa adzapulumutsa moyo wa wochimwayo ku imfa, ndipo adzakwirira machimo ambiri [a kusazindikira]" (Yakobo 5:15-20). Ngati mukufuna kukhululukidwa machimo anu, aulureni ndi kulapa, ndipo Mulungu wa moyo adzakukhululukirani ndi kukupanganinso watsopano. Ndikupemphera kuti mutero nthawi isanathe. Bwerani kwa Khristu tsopano pakunena pemphero ili!

AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.¹⁵ Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.¹⁶ Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wamtengo wapatali ndi cholinga choti

machimo anga onse akhululukidwe.¹⁷ Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,¹⁸ ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.¹⁹ Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.²⁰ Tsukani machimo anga ambirimbiri achoke onse mu mwazi wamtengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.²¹ Ndikudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.²² MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.²³ Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.²⁴ Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.²⁵

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.²⁶ Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a*

Mulungu, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.²⁷

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa M'busa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kupereka chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nkhokwe zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mudiye, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhale nonse mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

15 Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 16 Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 17 Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 18 Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 19 Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 20 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 21 Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 22 Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 23 Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 24 Aheb. 11:6 25 Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 26 Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 27 Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhani zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembereni.

Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078

Lama ya pemphero ndi uthenga maola 24: +1 (661) 252-5686 • +1 Fax (661) 252-4362

www.alamoministries.com • info@alamoministries.com

Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika kwa onse amene ali ku U.S.

amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zawo zonse

Mapemphero amachitika usiku uli wonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi Lamulungu nthawi ya 3 Koloko madzulo ndiponso

8 Koloko usiku ku Tchalitchi cha kudera la Los Angeles: 13136 Sierra Hwy., Santa Clarita, CA 91390, +1 (661) 251-9424

Magalimoto a ulere opita ndi kuchokera ku mapemphero amaperekedwa pa kona ya Hollywood Blvd. ndi Highland Ave.,

Hollywood, CA tsiku lili lonse nthawi ya 6:30 madzulo, Lamulungu lili lonse nthawi ya 1:30 madzulo ndi 6:30 usiku.

Mapemphero amachitika mu Mzinda wa New York Lachiwiri lili lonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi madera ena usiku okhaokha.

Chonde imbani foni kuti mumve zambiri: +1 (908) 937-5723. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PA MAPETO PA MAPEMPHERO ALI WONSE

Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.

Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo

Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira

Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa +1 (661) 252-5686.

M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).

MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.

Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati

mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:

© Copyright September 2010, 2015 All rights reserved World Pastor Tony Alamo © Registered September 2010, 2015

CHICHEWA/NYANJA—VOLUME 10800—COME UNTO CHRIST